COMPETITION AND FAIR TRADING COMMISSION

Just Competition, Fair Trading

Bungwe lowonetsetsa kuti mpikisano wa malonda ukuchita mwa chilungamo la CFTC lidakhazikitsidwa motsata lamulo lowonaza Mpikisano ndi chilungamo pa malonda. Cholinga cha lamuloli ndi kuwonetsetsa kuti Malonda akuchitika mopindulira chuma cha dziko, ogula komanso a Malawi onse.

Ntchito yabungweli ndi kuyang'anira, kuwunika, kuletsa ndi kupewa mchitidwe wina uliwonse omwe ungathe kusokoneza mchitidwe wa mpikisano wa chilungamo pa malonda. Zolinga zikuluzikulu zalamuloli ndi kulimbikitsa mpikisano pa malonda; kulimbikitsa dongosolo labwino; komanso kuteteza ogula kumbali ya chuma.

Kuphatikizana kwa Makampani a Malonda

Kuphatikizana kwa Makampani pa Malonda kumakhudza kwambiri malonda komanso ogula kumbali ya chuma. Kuphatikizana kukumachepetsa mpikisano komanso kumabweretsa kusakhazikika kwa mitengo ya malonda. Ochita malonda akuyenera kupempha chilolezo ku bungwe la CFTC asanalowe mu mgwirizano wakuphatikizana kwawo. Ngati alibe chilolezo cha bungweli, ndiye kuti m'gwirizano wawo ndi osavomerezeka.

Kodi zina ndi ziti zomwe zimatsutsana ndi mpikisano pa malonda?

Lamuloli limaletsa migwirizano ndi ziganizo zomwe zingasokoneze, kuletsa kapenanso kutsamwitsa dongosolo la mpikisano wabwino wokomela anthu onse m'Malawi munjira ina iliyonse. Zitsanzo zakachitidwe koletsa mpikisano pa malonda ndi monga izi:

- Tsankho Kulowa pa m'gwirizano womwe mfundo zake ndi zopanda chilungamo
- Kugulitsa katundu mophatikizana
- Osalola ena kuti azigulitsanawo katundu
- Kukhazikitsa mtengo umodzi pakati pa opikisana pa malonda
- Chinyengo ndi kubera pofuna kupeza mwayi woperekera katundu
- Migwirizano yogawana misika ndi ogula
- Kumemezana pofuna m'gwirizano
- Kugawana kakatundu pa msika
- Kukanisitsa kugulitsa malonda kwa anthu ena ofunisitsa kugula.
- Kugwirizana kukaniza ena kulowa mu m'gwirizano
- Kugwiritsa ntchito mphamvu zawo pa msika popondereza ena.

Just Competition, Fair Trading
Just Competition, Fair Trading

Mchitidwe wopanda chilungamo kwa ogula malonda

Mchitidwe wa malonda opanda chilungamo ndi omwe umabweretsa zipsinjo zochuluka kwa ogula. Machitidwe wopanda chilungamo kwawogula ndi monga awa:

- Kubisa kapena kuwononga katundu ndi cholinga chofuna kukweza mitengo ya katunduyo;
- Kukana kuchitapo kanthu pa katundu yemwe wapezeka ndi vuto kapena kuwonetsa mawu okana kubweza katundu pomwe mwagula;
- Kuyikapo katundu osiyana ndi yemwe amatsatsidwa;
- Kuchita zinthu mosokene zadala;
- Kugulitsa katundu wowononge ka kapena owopsa kwa anthu;
- Kuyika mfundo zosavomerezeka ndi zopanda chilungamo pa malonda.
- Kuchita malonda omwe phindu lochuluka likupita kwa munthu m'modzi ena akuvutika;
- Kuchita malonda omwe ali ndi nyambo;
- Kulonjeza kupereka mphotho koma wosafuna kupereka mphothoyo
- Kutsatsa malonda monama

Kodi ndingachite chiyani pomwe ndakhudzidwa ndi kachitidwe ka malonda kosokoneza mpikisano komanso kopanda chilungamo?

- Ogula kapena ogulitsa aliyense ali ndi ufulu okadandaula ku CFTC zokhudza m'chitidwe uliwonse wopanda chilungamo.
- Bungwela CFTC lidzawunika mokwanira kutilitsimikize ngati lamulo lowona chilungamo pa malonda laphwanyidwa.
- Potengera zotsatiraza ka uni uni, bungweli lidzachotsa dandauloli kapena lidzapereka dandauloli ku mabungwe ena okhudzidwa.
- Bungweli lidzathandiza ogula kuti abwezeredwe ndalama zawo kapena kusintha katundu.

Zilango

Wophwanya lamulo adzapereka chindapusa chokwana K500, 000 kapena ndalama yofanana ndi phindu lomwe lapangidwa pochita cholakwikacho, kapenanso kumangidwa kwa zaka zisanu ngati mulanduwo ndi waukulu.

Just Competition, Fair Trading

LUMIKIZANAN INAFE:

Lemberani kalata:

The Executive Director
Competition and Fair Trading Commission
1st Floor, Mpikisano House, Area 3
Off Mandala Road
Private Bag 332
Lilongwe 3
MALAWI

Kapena imbani lamya pa:

Lamya yolipira: +265 1 759506/7
Fax : +265 1 759522
Lamya yaulele: 80008333 (kuchoka kulamyaza MTL zokha)

Muthanso kutipeza ku:

Blantyre Office
Government Building
3rd Floor, Right Wing
Adjacent to Ministry of Industry, Trade and Tourism Offices
Blantyre

Email: competitioncommission@cftc.mw
consumer@cftc.mw
Website: www.cftc.mw

Just Competition, Fair Trading